CHIKONDI CHA MULUNGU



"Onani, chikondi chotere anatipatsa Atate."
— 1 Yohane 3:1

Mulungu Atate akutipempha kuti tione chikondi chotere, kapena kukula kwake kwa chikondi, chimene Iye ali nacho pa ife. Baibulo lonse limaika chidwi pa kukula kwa chikondi cha Mulungu Atate pa aliyense wa ife. Kusakhulupirira chikondi cha Mulungu pa ife kumalepheretsa ubale wathu ndi Mulungu. Kunali kusakhulupirira chikondi chachikulu cha Mulungu kumene kunayambitsa Satana panjira yake yotsikira pansi. (Onani Ezekieli 28:14-17.) Kunali

kusakhulupirira chikondi chachikulu cha Mulungu kumene kunakopa Hava kuti achimwe. (Onani Genesis 3:1-6.) Ndi kusakhulupirira chikondi chachikulu cha Mulungu kumene kumatisunga m'tchimo. Pokhapokha kudzera m'vumbulutso la chikondi chopanda malire cha Mulungu m'pamene tidzalowetsedwa mu ubale wachikondi ndi Mulungu umene uposa uliwonse umene takhala nawo mpaka pano.

Cholinga cha Satana chakhala kunyenga anthu za khalidwe lenileni la Mulungu. Satana afuna kuti tikhulupirire kuti Mulungu sali wachikondi monga momwe amanenera, ndipo akudziwa kuti ngati angatikhutiritse pa nkhani imeneyi, sitidzakonda Mulungu ndi mtima wathu wonse. Pokhapokha tikakhala ndi chithunzi choona cha chikondi cha Mulungu m'pamene tingamkonde mokwanira kuti tikwaniritse lamulo limene Yesu analitcha "lamulo lalikulu ndi loyamba," limene ndilo kukonda Mulungu ndi mtima wathu wonse. (Onani Mateyu 22:37, 38.)

KODI TINGACHIPEZE BWANJI CHIKONDI CHIMENECHO?

Yesu anati, "Ngati mukonda Ine, sungani malamulo anga." (Yohane 14:15) Maganizo omwewo akunenedwa mu vesi 23. "Ngati munthu akonda Ine, adzasunga mawu anga."

(Yohane 14:23) M'Baibulo la Chigriki, vesi 14 lamasuliridwa motere: "Ngati mukonda Ine, mudzasunga malamulo anga." (Jay P. Green's Greek Interlinear)

Vesi limeneli ndi mawu onena za chifukwa ndi zotsatira zake, osati lamulo. Yesu anati ngati timkonda Iye, chotsatira chachibadwa cha chikondi chimenecho nchakuti tidzasunga malamulo ake. Ngati sitikonda Mulungu, sitingathe, ndipo sitidzasunga, malamulo ake.

Yesu anati, "Uzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi nzeru zako zonse. Ili ndi lamulo lalikulu ndi loyamba. Ndipo lachiwiri lofanana nalo ndi ili, Uzikonda mnansi wako monga udzikonda iwe mwini. Pa malamulo awa awiri mapachikidwa chilamulo chonse ndi aneneri." (Mateyu 22:37-40)

Ngati tikonda Mulungu ndi mtima wathu wonse, sitidzakhala ndi milungu ina pamaso pake. Sitidzapembedza fano losema, kuswa Sabata, kapena kutchula dzina lake pachabe. Ngati tikonda mnansi wathu monga tidzikonda ife eni, sitidzamupha, kumuba, kumunamizira umboni wonama, kusirira katundu wake, kuchita chigololo, kapena kusalemekeza makolo athu.

Chifukwa chake Paulo anatha kunena mawu awa motsimikiza: "Musakhale ndi mangawa

kwa munthu aliyense, koma kukondana wina ndi mnzake; pakuti iye amene akonda mnzake wakwaniritsa chilamulo.... Chikondi sichichitira mnansi choipa; chotero chikondi ndicho chokwaniritsa chilamulo." (Aroma 13:8-10)

Kukonda Mulungu ndi mtima wathu wonse ndilo lamulo lalikulu ndi loyamba. Nzodziwikiratu kuti sungathe kuswa lamulo limeneli ndi kukhalabe wosunga malamulo a Mulungu. Monga tikuonera bwino, ngati tikuyesetsa kusunga malamulo a Mulungu, cholinga chathu choyamba ndi chapamwamba koposa ndicho kukonda Mulungu ndi mtima wathu wonse, nzeru, moyo, ndi mphamvu zathu zonse. Koma kodi cholinga chimenechi chingakwaniritsidwe bwanji?

Yohane analemba, "Ife timkonda Iye, chifukwa Iye anayamba kutikonda ife." (1 Yohane 4:19) Chifukwa chokhacho chimene chaperekedwa cha munthu kukonda Mulungu ndi ichi, "chifukwa Iye anayamba kutikonda ife." Ngati tifuna kukonda Mulungu, tiyenera choyamba kuona chikondi chake pa ife. Monga momwe tizindikira ndi kuyamikira chikondi cha Mulungu pa ife, momwemonso chikondi chathu pa Mulungu chidzakhala. Ngati uona kuti Mulungu amakukonda pang'ono chabe,

ndiye kuti chikondi chako pa Iye chidzakhala chochepa kwambiri. Ngati uona kuti Mulungu amakukonda kotero kuti anapereka chimene chinali chamtengo wapatali koposa kwa Iye, Mwana wake wobadwa yekha, ndiye kuti chikondi chako pa Iye chidzakhala chachikulu.

KODI TINGACHIDZIWE BWANJI CHIKONDI CHA MULUNGU?

"Umo chaonetsedwa chikondi cha Mulungu mwa ife, kuti Mulungu anatuma Mwana wake wobadwa yekha kudziko lapansi, kuti tikhale ndi moyo mwa Iye. Umo muli chikondi, sikuti ife tinakonda Mulungu, koma kuti Iye anatikonda ife, natuma Mwana wake akhale chiombolo cha machimo athu." (1 Yohane 4:9, 10) Mulungu waonetsa chikondi chake chachikulu mwa kupereka Mwana wake wobadwa yekha.

"Ndipo ife tadziwa, ndipo takhulupirira chikondi chimene Mulungu ali nacho pa ife. Mulungu ndiye chikondi; ndipo iye wokhala m'chikondi akhala mwa Mulungu, ndi Mulungu akhala mwa iye. M'menemo chikondi chathu chikhala changwiro." (1 Yohane 4:16, 17) Chikondi chathu pa Mulungu chimakhala changwiro mwa kudziwa, kukhulupirira, ndi kukhala m'chikondi chake pa ife, chakuti anapereka Mwana wake wobadwa yekha.

Tiyenera choyamba kuzindikira m'mene tingadziwire chikondi cha Mulungu, kuti tichikhulupirire ndi kuchilingalira nthawi zonse, zimene zidzapangitsa chikondi chathu pa Iye kukhala changwiro. "Umo tizindikira chikondi cha Mulungu, popeza Iyeyo [Yesu] anapereka moyo wake chifukwa cha ife." (1 Yohane 3:16) Kuti tidziwe chikondi cha Mulungu pa ife, tiyenera kuyang'ana m'mene anaperekera Mwana wake kuti apereke moyo wake chifukwa cha ife.

MASAUTSO A KHRISTU

Marko analemba za usiku umene unatsogolera imfa ya Khristu: "Ndipo anafika pamalo dzina lake Getsemane; ndipo ananena kwa ophunzira ake, Khalani pano, pamene ndipemphera. Ndipo anatenga pamodzi naye Petro ndi Yakobo ndi Yohane, nayamba kudabwa kwambiri, ndi kusauka mtima ndithu. Ndipo ananena nawo, Moyo wanga uli wa chisoni chambiri kufikira imfa; khalani pano, nimudikire [mumvetsere mosamala kwambiri]. Ndipo anapita patsogolo pang'ono, nagwa pansi, napemphera kuti, ngati nkutheka, nthawiyo impitirire." (Marko 14:32-35) Yesu anapempha ophunzira ake kuti ayang'anire zimene zinali kuchitika, chifukwa anafuna kuti adziwe ndi kukhulupirira chikondi chimene Mulungu

ali nacho pa iwo, kuti chikondi chawo pa Mulungu chikhale changwiro.

Tiyeni tione zimene zinachitika m'munda wa Getsemane. "Panali chinachake chimene chinali kuchitikira Yesu chimene chinampangitsa kunyansidwa ndi zimene anali kumva mumtima mwake, ndipo zimenezo zinamuopsa kwambiri. Kodi zimene anali kumvazo zinali zotani?"

Yesaya ananenera, "Yehova anaika pa Iye mphulupulu [pamodzi ndi kulakwa] ya ife tonse." (Yesaya 53:6) Yesu anamva manyazi amene timamva tikachimwa, koma ochulukitsidwa kambirimbiri. Zimenezi zinadzetsa kulekana pakati pa Mulungu ndi Iye. "Koma mphulupulu zanu zakulekanitsani inu ndi Mulungu wanu, ndipo zochimwa zanu zakubisirani nkhope yake, kuti Iye sadzamva." (Yesaya 59:2)

Mulungu amatikondadi kotero kuti anapereka Mwana wake wobadwa yekha, ndipo afuna kuti tione, kapena kuti tilingalire nthawi zonse, choonadi chamtengo wapatali chimenechi. "Pakuti chikondi cha Khristu chitikakamiza [chitiumiriza kapena chimadzaza maganizo athu onse]." (2 Akorinto 5:14) Maganizo athu onse ayenera kudzazidwa ndi choonadi chodabwitsa chakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero kuti analola Mwana

wake wobadwa yekha kumva kulakwa kwathu ndi kuzunzika ndi zotsatira za kulakwa kumeneko kuikidwa pa Iye.

Yesaya analemba, "Mtima wokhazikika pa Inu mudzausunga mu mtendere weniweni; chifukwa ukhulupirira Inu." (Yesaya 26:3) Mulungu adziwa kuti ngati tilingalira chikondi chodabwitsa chimene ali nacho pa ife, chidzatiumba ndi kutisintha monga palibe china chingachite. Ngati tidzakhala tikuzindikira nthawi zonse chikondi chimene Mulungu ali nacho pa ife, ndi kuyamikira chikondi chimenecho, potsiriza tidzanyansidwa ndi tchimo kotero kuti tidzakana kulilola kukhalabe mwa ife. Tingathe kugonjetsa tchimo ndi thandizo la Mulungu.

"Pakuti chilichonse chobadwa mwa Mulungu chigonjetsa dziko lapansi; ndipo ichi ndi chigonjetso chimene chigonjetsa dziko lapansi, ndicho chikhulupiriro chathu. Ndani iye wogonjetsa dziko lapansi, koma iye wokhulupirira kuti Yesu ndiye Mwana wa Mulungu?" (1 Yohane 5:4, 5) Pali chinachake m'kukhulupirira kuti Yesu ndiye Mwana wa Mulungu chimene chimatithandiza kugonjetsa tchimo. (Onani 1 Yohane 2:15-17.) Popeza kukhulupirira kuti Yesu ndiye Mwana wa Mulungu kumatithandiza kugonjetsa tchimo, kodi ukuganiza kuti Satana angayese

kupotoza choonadi chakuti Yesu ndiye Mwana wa Mulungu? Ndithudi angatero. Ngati tiyembekeza kugonjetsa dziko lapansi, tiyenera kukhulupirira kuti Yesu ndithu ndiye Mwana wobadwa yekha (amene anabadwadi) wa Mulungu, ndi kuti Mulungu anampereka chifukwa cha ife.

"Iye wokhulupirira Mwana wa Mulungu ali nawo umboni mwa iye yekha; iye wosakhulupirira Mulungu wamyesa Iye wonama; popeza sanakhulupirira umboni umene Mulungu wachitira Mwana wake." (1 Yohane 5:10) Mulungu anati, "Uyu ndiye Mwana wanga wokondedwa, amene ndikondwera naye; mverani Iye." (Mateyu 17:5) Mulungu anati Yesu Khristu ndiye Mwana wake wobadwa yekha; usalole munthu aliyense akuuze zina.

"MPHATSO YA MULUNGU: MWANA WAKE"

"Yesu, polankhula za Iye yekha, anati, "Pamene panalibe madzi akuya, ndinabadwa ine [ndinabadwadi]; pamene panalibe akasupe odzala ndi madzi. Asanakhazikike mapiri, zisanakhale zitunda, ndinabadwa ine." (Miyambo 8:24, 25) Liwu la Chihebri limene lamasuliridwa pano kuti "ndinabadwa" limatanthauza "kubadwa" (Gesenius' Hebrew Lexicon). Yesu ndiye Mwana weniweni wa Mulungu, amene

anabadwa kumwamba dziko lapansi lisanakhalepo.

"Pokhapokha podziwa ndi kukhulupirira kuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero kuti anaperekadi Mwana wake wobadwa yekha, m'pamene chikondi chathu pa Mulungu chingakhale changwiro ndithu. Chifukwa chake, pokhapokha podziwa ndi kukhulupirira kuti Mulungu anatuma Mwana wake wobadwa yekha kudziko lapansi, m'pamene tingasunge malamulo ake."

"Padzakhala gulu la anthu m'masiku otsiriza amene adzakonda Mulungu ndi mtima wawo wonse. Iwo adzadziwa chikondi cha Mulungu chimene chiposa chidziwitso. Adzazindikira kuti Mulungu amatikonda kwambiri kotero kuti anapereka Mwana wake wobadwa yekha. Gulu la anthu limeneli limadziwika kuti 144,000. Iwo ndiwo amene alandira chisindikizo cha Mulungu. (Onani Chivumbulutso 7:1-4) Iwo adzakhala opanda chilema. "Ndipo ndinapenya, taonani, Mwanawankhosa alikuimirira paphiri la Ziyoni, ndi pamodzi naye zikwi zana limodzi mphambu makumi anai mphambu zinai, okhala nalo dzina la Atate wake lolembedwa pamphumi pawo. ... Ndipo m'kamwa mwawo simunapezeka chinyengo; pakuti ali opanda chilema pamaso pa mpando wachifumu wa

Mulungu." (Chivumbulutso 14:1, 5) Iwo sadzavomera kulandira chizindikiro cha chilombo, ndipo adzapulumutsidwa ku miliri yonse imene idzagwera dziko lapansi."

"Anthu awa adzazindikira chikondi cha Mulungu kufikira kuti sadzachimwa. "Otsala a Israele sadzachita chosalungama, kapena kunena mabodza; ndipo lilime lonyenga silidzapezeka m'kamwa mwawo; pakuti adzadya nadzagona pansi, ndipo palibe wina adzawaopsa." (Zefaniya 3:13) Iwo ndiwo umboni wa Mulungu wakuti munthu angathe kugonjetsa tchimo. Ine ndikufuna kukhala mmodzi wa chiwerengero chimenecho.

Padzakhalanso gulu lina m'masiku otsiriza; gulu limene lidzalandira chizindikiro cha chilombo. Padzakhala magulu awiri okha. Sipadzakhala gulu lapakati. Mwina udzalandira chizindikiro cha chilombo, kapena chisindikizo cha Mulungu. Gulu limene lilandira chizindikiro cha chilombo silidzagonjetsa tchimo. Iwo adzapitirizabe kukhala m'machimo amene anadzisankhira. Kodi mapeto awo adzakhala otani? "Taonani, tsiku la Yehova lilinkudza, laukali, ndi mkwiyo ndi kupsa mtima koopsa, kuti lisandutse dziko bwinja, ndi kuwononga ochimwa ake m'menemo." (Yesaya 13:9) Ochimwa adzawonongedwa pamene Ambuye adzabwera. Iwo adzafuula kuti matanthwe

awagwere, kuwabisa pamaso pa Ambuye. Tchimo lililonse lokondedwa limene sitinalape ndi kulisiya lidzatigwetsa tsiku limenelo ndi kutichititsa kuwonongedwa. "Wobisa machimo ake sadzaona mwayi; koma wakuwavomereza nawasiya adzachitidwa chifundo." (Miyambo 28:13) Chonde, konzekerani nthawi isanathe!

Padzatuluka chilengezo Ambuye atatsala pang'ono kubwera, ndipo milandu yonse idzaweruzidwa, kaya kwa zabwino kapena kwa zoipa. "Iye wosalungama, achitebe zosalungama; ndi iye wodetsedwa, adetsedwebe; ndi iye wolungama, achitebe cholungama; ndi iye woyera mtima, akhale woyerabe. Taona, ndidza msanga; ndipo mphotho yanga ili ndi Ine, kubwezera munthu aliyense monga mwa ntchito yake." (Chivumbulutso 22:11, 12) Ichi ndi chenjezo lalikulu. Chonde, khalani okonzeka!